Kodi Zithunzizi Zikusiyana Pati?

Kodi mungatchule zinthu zitatu zimene zikusiyana pakati pa chithunzi A ndi chithunzi B? Lembani mayankho anu m'mizere ili m'munsiyi, ndipo malizitsani kujambula zithunzizi pozikongoletsa ndi chekeni. ZOKUTHANDIZANI: Werengani 1 Samueli 16:1-3, 6-13.

1 .....

2 .....

3 .....

4. Kodi chithunzi cholondola n'chiti, A kapena B?

KAMBIRANANI: Kodi Yehova amaona chiyani mwa munthu? Kodi Baibulo limatanthauza chiyani likamanena kuti 'Yehova amaona mumtima'? ZOKUTHANDIZANI: Werengani Yeremiya 17:10. Kodi maonekedwe a munthu ndi ofunika kwambiri kwa Yehova? ZOKUTHANDIZANI: Werengani Miyambo 11:22; 31:30; 1 Petulo 3:3, 4. Kodi ndi makhalidwe ati amene angakuchititseni kuti mukhale wokongola kwa Mulungu? ZOKUTHANDIZANI: Werengani Luka 10:27; 2 Petulo 1:5-8.

ZOTI BANJA LICHITIRE PAMODZI: Werengani Agalatiya 5:22, 23. Lembani khalidwe lililonse papepala lakelake. Sankhani munthu mmodzi m'banja mwanu n'kumumata kapepala kamodzi pachipumi. Munthuyo asaone zimene zalembedwa pa kapepalako. Muzimufunsa mafunso osiyanasiyana okhudza khalidwelo n'cholinga choti anene khalidwe limene lili pa kapepalako. Ena onse m'banjamo aziyankha kuti eya wofunsidwayo akayankha molondola kapena ayi akalakwitsa.



Nkhani zina zakuti "Zoti Banja Likambirane" mungazipeze pa adiresi yathu ya pa Intaneti ya **www.jw.org/cn**

1. Pachithunzi china pali mbuzi pamene chinacho pali ng'ombe. **2.** Pachithunzi china pali mtsikana pamene chinacho palibe. **3.** Pachithunzi china pali kathumba ka chikopa kolkamo vinyo pamene chinacho pali nyanga ya mafuta. **4.** B.

www.jw.org © 2012 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania